NYA_TTB_0945_20161111_**script**

Ahebri : Chiyambi cha buku

Mutu : Mau otsogolera buku la Ahebri

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau a Mulungu opezeka pa Luka 8:17, akuti, “Pakuti palibe chinthu chobisika, chimene sichikhalachoonekera; kapena chinsinsi chimene sichidzadziwika ndi kubvumbuluka.”

Lero tikuyamba buku latsopano la m’Chipangano Chatsopano lotchedwa Ahebri.Ili, ndilo buku lomwe lidautsam’tsutso pakati pa anthu olemba ambiri, a Chipangano Chatsopano. Kunena kuti palibe gawo lina la mabuku am’Baibulo lomwe maganizo osiyana-siyana alandiridwa koposa buku la Ahebri. Mtsutso umenewu, wakhudza kwambiri za munthu wolemba bukuli, nthawi ndi malo komwe bukuli linalembedwera, likukamba za yani, mpingo komwe kalatayi ikutumizidwa.Komanso m’bukuli mulibe zizindikiro za nthawi monga zomwe zimathandizira kuzindikira nthawi pomwe kalatayi inalembedwera monga momwe, zimaoneka m’makalata a Paulo. Ndiye nkofunika kuzindikira kuti m’kalata imeneyi, muli

zinthu zambiri zomwe ndi zobvuta kuzimvetsa, pamene tifanizira ndi makalata ena m'Chipangano Chatsopanochi, koma ndimomwe tingapezechitonthozo chokwanira cha Mzimu wa Mulungu.

Tere, tamvani maganizo ya anthu atatu awa, amene akunena za buku limeneli.

Poyamba a G. Campbell Morgan, m'buku lawo lotchedwa God's Last Word to Man: akunena kuti, "Kalata iyi, yolembedwakwa Ahebri, ndiyofunika kwambiri lero lino chifukwa muli chidziwitso chachikulu cha Kristu."

Ndipo bambo E. Schuyler, ananena kuti, "Kalata yopita kwa Ahebri, ndi buku limodzi mwa mabuku ofunika kwambiri m'Chipangano Chatsopano, popeza muli ziphunzitso zikulu-zikulu za moyo wachikristu. Bukuli muli choona cha Mulungu choonekera bwino-bwino kotero kuti pamene inu muwerenga, zimakhala ngati kuti mukupumampweyawa Kumwamba kweni-kweni. Ndiye pamene munthu asanthula bukuli, kumakhala kudyerera nyama ya mnofuyauzimu.Ndipo pakumvera ziphunzitso zake, imakhala njira yochokapaumwana ndi kufika pokulam'chidziwitso cha choona cha chikristu ndi Kristu mwini, chimene chidzatifikitsapokula kwa

mphumphu." Ndiye poumbamkota mau onsewa, mkuluyu, akunenetsa kuti, "Chiphunzitso chachikulu m'kalata imeneyi, yopita kwa Ahebri ndi chakuti Ambuye wathu,akuonetsedwa kuti ndiye Wansembe Wamkulu, mwaulemerero wa Kristu, Mwana wa Mulungu ndi Mwana wa munthu."

Ndipo Sir Robert Anderson, m'buku lawo lotchedwa "The Hebrews Epistle in the Light of the Types" momwe akunena kuti, "Mpingo wokhulupirira Kristu ndiwo mpesa weni-weni. Ichi, ndichiphunzitso chomwe akristu ambiri m'mipingoyosinthika (Reformation), amakhulupirira.Ichi, ndichiphunzitso cha mau a Mulungu chomwe chikuonetsedwamobveka bwino kuti Kristu ndiye Mpesa weni-weni, Israyeli ndiye mphesa (chipatso chake), popeza Mulungu sanataye anthu ake, amene anawadziwa kale."

Wokondedwa anzanga apaulendo, taonani ngakhale kuti anthu ochuluka akuyamikira kalata imeneyi, koma siinalandiridwe ndi mpingo wakumaiko aku madzulo (Europe) kwa nthawi yaitari. Ichi, ndichifukwa chakuti mpingo sunagwirizane ndi pfundo yakuti Mulungu sanataye anthu ake, amene anawadziwa kale.Ndiye pachifukwa chimenechi, mpingowo umafuna kuchotsa Israyeli pa

mau amenewa. Kunena kuti mpingowounabvomerezamalonjezo onse amene Mulungu anapereka kwa Israeli, kuzindikira momwe malonjezanowoangawakhudzire iwowo, koma anali kukana zolinga za Mulungu pa mtundu, wa Israyeli.

Ndiye zotsatira zake m'zakuti mpingo m'masiku amenewo, unaimapatsankho la mitundu ya anthu, nazunza mtundu wa a Yuda koposa mitundu ina yonse. Tsono tikupeza kuti ndichinthu cholakwakwakukulukulimbikitsa ganizo lakuti Mulungu anathana nawo kale a Yuda, ndipo kalata iyi, itithandizakuona kuti m'Hebri ndi m'Hebri ndithu, ngakhale pamene atembenuka mtima akhalabem'Hebri ndithu. Ndikutanthauza kuti pamene inu mutembenuka mtima kukhala mkristu, sizitanthauza kuti mtundu wanu wasintha ayi, koma mumangoponyedwamgulu la anthu okhulupirira, lotchedwa mpingo. Tere, ndichifukwa chake Mulungu lero lino akuitana anthu onse achiYuda ndi amitundu ina, kuti atchulidwe dzina lake. Pamene chinthu ichi, chidzakwaniritsidwa, ndipo pamene Mulungu adzakwatula mpingo wake kuuchotsa m'dziko lapansi lino.Apa, ndipo pamene Mulungu, adzakwaniritsazolinga zake ndi mtundu wa Israyeli, pofuna

kukwaniritsa malonjezo ake kwa iwowa, komanso kukwaniritsa malonjezo ake, kwa anthu amitundu ina podzeramwaiwowa.

Ndiye pano tafika, tiyenera kunena kuti pamene tiganizira za munthu amene analemba kalata iyi, yopita kwa Ahebri, tipezadi kuti ndilo funso lomwe lakhala lobvutakuyankhakwambiri. Tere, ngakhale Baibulo la Authorized Version, linalemba kuti kalata ya Ahebri, inalembedwa ndi Paulo, ma version a Revised ndi ena, anayesa kukonzaganizoli ponena kuti wolemba wa kalata imeneyi, sakudziwika. Kutsindika kuti pamene inu mutenga nthawi yaikulu kusanthula mau a Mulungu, mupeza kuti palibe m'gwirizano pa nkhani ya munthu amene analemba kalata imeneyi.

Tsono nkhani ikunena kuti anthu ambiri kuphatikizapo anthu odziwika bwino pa kumasulira mau a Mulungu a John Calvin ndi Martin Lurther, akunenetsa kuti Paulo sanalembe kalata imeneyi. Koma tikunenetsa kuti kukangana pa munthu amene analemba kalata iyi, sichinthu chofunika kwambiri, koma kuzindikira kuti kalata yopita kwa Ahebri, ndigawo limodzi la mau a Mulungu amene ndi obvomerezeka.

Tsono ngakhale kuti kulembedwakwa kalatayi ndi Paulo sikulikobvomelezeka ndi anthu ambiri, koma pali umboni wochuluka wochokera m'kati mwa kalatayi ndi kunja kwake, umene ukuonetsabe kuti Paulo ndiye amene analemba kalata imeneyi. Taonani umboni umene uli pa Ahebri 10:34, umene ukuonetsa kuti wolembayu anali m'ndende. Pachifukwa chimenechi, tikuganiza kuti ayenera kukhala kuti ndiye analemba kalatayi panthawi yomwe iye anali m'ndende, nanena kuti, "Pakuti munamva chifundo ndi iwo a m'ndende, ndiponso mudalolamokondwerakulandidwa kwa chuma chanu, pozindikira kuti mulinacho monga chuma choposachachikhalire." Komanso taonani pamene tiwerenga pa Ahebri 13:24, tipeza mau akuti, "Lankhulani atsogoleri anu onse ndi oyera mtima onse. Akulankhulani iwo a ku Italiya."Tere, mau amenewa ndi amene akudzetsanso ganizo lakuti kalata iyi, iyenera kuti inalembedwa ndi Paulo pamene anali ku Italy.Ndipo panthawi imeneyo, zikuonetsa kuti anali ndi Timoteo ngati mzake amene anali kuyenda naye paulendo. Awa, ndiwo mau amene ali pa Ahebri 13:23, amene akuti, "Zindikirani kuti m'bale wathu, Timoteo wamasulidwa; pamodzi ndi iye, ngati akudza msanga, ndidzakuonani inu."

Komanso pamene tiwerenga pa 2 Petro 3:15-16, tipeza mau akuti, “Ndipo yesani kulekerera kwa Ambuye wathu chipulumutso monganso m’bale wathu wokondedwa Paulo, monga mwa nzeru zopatsidwa kwa iye, anakulemberani; monganso m’makalata ake onse pokamba momwemo za izi; m’menemo muli zina zobvuta kuzizindikira, zimene anthu osaphunzira ndi osakhazikikaapotoza, monganso atero nawo malembo ena, ndi kudziononga nawo eni.” Tsono tikunena kuti palibenso wolemba wina amene analemba kalata kwa Ahebri, koma Paulo yekha.

Ndiye mwina inu muli kufunsa kuti, Paulo wakhala akulemba dzina lake m’makalata ake onse, kodi pali chifukwa chanji lero kuti asalembe dzina lake m’kalata ino? Yankho likuti, Paulo pozindikira kuti ndiye Mtumwi kwa anthu amitundu ina, amene anali kudana ndi a Yuda, anayenera kuchotsa dzina lake m’kalata iyi, chifukwa akanapandakutero, a Yudawosakanakhala ndi chidwi chowerenga bukuli chifukwa cha udani wawo ndi anthu amitundu ina. Komanso pali chifukwa chakuti a Yuda ndiwo aja anali kunena kuti Paulo ndiye anali woukira chipembedzo chawo monga tiwerenga pa Machitidwe Atumwi 21:27-28, pamene anati, “Ndipo pamene

masiku asanu ndi awiri anati amarizidwe, a Yuda a ku Asiyapomuona iye m'Kachisi, anautsa khamu lonse la anthu, namgwira, napfuula, amuna a Israyeli, tithandizeni; ameneyu ndi munthu uja anaphunzitsa onse ponsepoponenera anthu ndi chilamulo, ndi malo ano; ndiponso anatenga a Helene nalowa nawo m'Kachisi, nadetsa malo ano oyera." Tere, mwa mau awa, kunali kobvuta kuti Paulo aulule dzina lake m'kalata iyi, popeza ndiye munthu amene amatchedwa woukira chilamulo ndi miyambo yansembe yachipembedzo chawo.Komanso ndiye anali kutengedwa kuti ndiye wodetsa Kachisi wawo popeza analowa ndi a Helene m'kachisimo.Ndiye pofuna kupereka Uthenga wa Kristu wodzudzula ndi wolimbikitsa a Yuda wotembenuka mtima, anayenera kulemba kalata iyi, mosaonetsa dzina lake.

Tsono pamene tifufuza za cholinga cha kalata iyi, tipeza kuti panali cholinga chofuna kudziwitsa ndi kutsimikiza za chiweruzo chomwe chikufotokonzedwa momveka bwino m'makalata a Uthenga Wabwino koposa momwe chilamulo chinena. Ndiye poonakuti a Yuda amenewa, anamangiririkakwambiri ku miyambo ya chilamulo, chimene chinapangitsa kuti ngakhale a Yuda amene

anatembenuka mtima abwerere ku miyambo imeneyi, kunali koyenera kupeza njira ina yamphamvu monga iyi, kuwachotsakuchikhulupiriro chimenechi. Tere, kalata iyi, ndiyo imene inalembedwa mwanjira yofunakuwakopa Ahebri kuti akhazikikem'chikhulupiriro cha chiphunzitso chachikristundikutiakhoze kupilira kumasautso onse amene angadze chifukwa cha kuchoka pamiyambo yawo. Pachifukwa chimenechi, tikuona kuti Mtumwi Paulo akukamba zambiri zokoma za Ambuye wathu Yesu Kristu, amene ali mwini wa Uthenga Wabwino. Kulimbikitsa Ahebriwokuti ayenera kumchitira ulemu Kristu wopambana koposa zina zonse.Tsono kalembedweka kalata iyi, kakusiyana ndi momwe makalata ena aja analembedwera. Tikunena kuti mu kalata iyi, mulibe zinthu zina zokometsera zofuna kukopa anthu amitundu ina, koma anangopereka Uthenga Wabwino monga momwe uli. Kutsindika kunena kuti Paulo mu kalata iyi, analidi m'Yuda kuti apindule a Yuda. Iyi, ndiyo nkhani yomwe adanena pa 1 Akorinto 9:20, pamene adanena kuti, "Ndipo kwa a Yuda ndinakhala monga m'Yuda, kuti ndipindule a Yuda..."Tere, kalembedwe aka ndiko kamenekakuonetsadi kuti

Paulo anali kufuna kupindula a Yuda okhala mu Alexandria ndi m'Yerusalemu yense.

Cholinga china cha kalata iyi, chinali chofuna kuonetsa kupambana kwachikristupakufanizira ndi chipembedzo cha chiyuda (Judaism). Kunena kuti Paulo akuonetsa kuti chikristu ndicho choposachiYuda chifukwa amene anadza nacho (Kristu) ndiye Wamkulu woposa angelo ndi Mose, amene anadza ndi malamulo, momwe utumiki wake ndi nsembe zake ndizosakwanira pachipulumutso cha munthu. Kutsimikiza kuti Mose ndi a nsembe akale anali kuimira Kristu Wansembe Wamkulu. Tere, ndichifukwa chake m'bukuli Paulo akuchenjeza a Yuda wotembenuka mtima kuti, sayenera kubwerera m'mbuyo pamene aona akristu akuzunzika, popeza a Roma sanadane nacho chi Yuda.

Tsono cholinga china chachikulu cha kalata iyi, chinali chakuti a Yuda, amene anatembenuka mtima atetezedwe ku mulandu wakuti anaukira chikhulupiriro cha chipembedzo chawo. Ndiye ndichifukwa chake wolembayuakufananitsazipembedzo ziwirizi, ndi momwe moyo wa akristu achi Yuda ukhoza kukhudzidwira. Komanso wolembayu akulimbikitsa akristu achiYudapakuonetsa

kupambana kwa chipembedzo chachikristupofanizira ndi chipembedzo cha chiYuda. Ndipo akunenetsa kuti miyambo ndi nsembe zonse zomwe zinali kuperekedwa, zinali zakutha ndipo kuti nsembezo zinali kuimira Kristu, amene aliwamuyaya.

Kalata iyi yolembedwakwa Ahebri, ndi ina mwa makalata ofunika kwambiri yomwe ikufanana ndi kalata yolembedwa kwa Aroma. Ndiye pamene inali kulembedwakwaAhebriwa panali cholinga chofuna kuthandiza a Yuda, amene anatembenuka mtima kuti asabwerere ku chipembedzo chawo Chakale cha chiYuda. Komanso panali lingalirolofunakuteteza anthuwa kuti asapangitsechikristu kukhala chiYuda ayi, popeza akristu ena a chiYuda anali kulingalira zophatikizazipembedzo ziwirizi, kukhala chimodzi.Iyi, ndiyo nkhani yomwe yiri pa Ahebri 13:22, imene ikuti, “Koma ndidandaulira inu, abale, lolani mau a chidandauliro; pakutinsondalembera inu mwachidule.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, pachifukwa chimenechi, a Yuda komanso wokhulupirira onse, kudzera m’kalata iyi, akulimbikitsidwa kuti palibe kubwerera m’mbuyo kapena kupitiliza chipembedzo cha chiYuda popeza Kristu ndiye Wansembe

Wamkulu ndi wopambana ena onse, amene anadza iwo asanafike. Kutsindika kuti anthu okhulupirirawa ayenera tsopano kuona Kristu, amene mwazi wake, kuuka kwa akufa kwake, ndi kukwera Kumwamba kwake ndiko kumene kunatsegula njira yolowa m'Kachisi woona wa Mulungu. Ndiye pamene azindikira kufunika ndi kupambana kwachikristu, wokhulupirira ayenera kukhala ndi mphamvu yogonjetsamayesero, aime nji m'nkhondoyauzimu ndi kupirira pakutsata njira yatsopano komwe iwo anapereka miyoyo yawo. Kutsindika kuti ngati wokhulupirirawo sangathe kuyenda m'moyo wachipambano, adzakumana ndi chiweruzo monga chomwe anakumana nacho Ahebri m'chipululu muja.

Pano ndipofunikanso kupereka nthawi yomwe kalatayi inalembedwera, pofuna kutsimikiza kuti Paulo ndiye analembadi kalatayi. Anthu olemba ambiri akhala akupereka maganizo osiyana-siyana, panthawi pomwe kalata iyi, inalembedwa: ena, akuti inalembedwa m'chaka cha A.D. 70 pamene ena akupereka chaka cha A.D. 85, A.D. 96. Koma pamene muwerenga kalata iyi, mupeza kuti inalembedwa pamene Kachisi wa m'Yerusalemu anali akanalipo. Pachifukwa chimenechi ndikoyenera kutsimikiza kuti

Paulo analemba kalata iyi, chisanakwane chaka cha A.D. 70 popeza m'chaka cha A.D. 70 ndipamene Titowaku Roma anaononga Kachisi, pamene Paulo anali atafa kale.

Tsopano tiona ndondomeko ya ziphunzitso zomwe zikupezekam'bukuli.

1. Kristu ndiye wopambana ziphunzitso za m'Chipangano Chakale, chapters 1-10
   A. Kristu ndiye Wamkulu ndi aneneri, chapters 1:1-3
   B. Kristu ndiye Wamkulu ndi angelo, chapters 1:4-2:18
      i. Umulungu wa Kristu, chapter1:4-14
      ii. Umunthu wa Kristu, chapter 2:1-18, chizindikiro choyamba cha tsoka, pakuchoka pamaso pa Mulungu, 2:1-4
   C. Kristu ndiye Wamkulu ndi Mose, chapter 3:1-4:2, chizindikiro chachiwiri, pakukaikira Kristu, chapters 3:7-4:2
   D. Kristu ndiye Wamkulu ndi Yoswa, chapter 4:3-13
   E. Kristu ndiye Wamkulu mwa unsembe wa a Levi, chapters 4:14-7:28

i. Kristu ndiye Wansembe wathu Wamkulu, chapter 4:14-16

ii. Kodi wansembe ndani? Chapter 5:1-10, chizindikiro chachitatu pakusamvetsetsa, chapter 5:11-14, chizindikiro chachinayipakuchoka pamau a Mulungu, chapter 6:1-20

iii. Kristu ndiye Wansembe Wamkulu monga dongosolo la Melikizideki, chapter 7:1-28

a. Kristu ndiye Wansembe wamuyaya, chapter 7:1-3

b. Kristu ndiye Wansembe Wolungama, chapter 7:4-22

c. Kristu mu Umunthu wake ndi muUnsembe wake ndi wamuyaya, chapter 7:23-28

F. Kristu monga Wansembe wathu Wamkulu, amatumikira m'Kachisi wa m'Mwamba, pamapanganookhalitsaomangidwa pa malonjezookoma, chapters 8:1-10:39

i. Kachisi weni-weni, chapter 8:1-5

ii. Chipangano Chatsopano ndicho chabwino koposa Chakale, chapter 8:6-13

iii. Kachisi watsopano ndiye apambana wakale, chapter 9:1-10

iv. Nsembe yoposa zonse, chapters 9:11-10:18

v. Chilimbikitso, chapter 10:19-25, chizindikiro chachisanu pakunyozera Kristu, chapter 10:26-39

II. Kristu ndiye amapereka ntchito ndi zinthu zokoma, chapters 11-13

A. Chikhulupiriro, chapter 11:1-40

B. Chiyembekezo, chapter 12:1-29

i. Mkristu ali pa makani a liwiro, chapter 12:1-2

ii. Akristu ali pa mpikisano ndi mkangano, chapter 12:3-14, chizindikiro cha chisanu ndi chimodzi chakukana Kristu, chapter 12:15-29

C. Chikondi, chapter 13:1-6

i. Chinsinsi cha moyo wa wokhulupirira, chapter 13:1-6

ii. Moyo wodalirana wa wokhulupirira, chapter 13:7-14

iii. Moyo wauzimu wa wokhulupirira, chapter 13:15-19

iv. Mau otseka buku, chapter 13:20-25

Kwalerotilekeza pano ndipo tinali kusanthula mau otsogolera buku la Ahebrilomwe ndibukulina lofunika kwambiri la m'Chipangano Chatsopano.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!